PHUMZIRO LA 43

1. Kodi Mulungu anapereka chilango chotani kwa mitundu khumi ya ku Isirayeli?
-Mulungu anaŵatumiza Asiliya kukayiputa mitundu khumi ya ku Isirayeli ndikuŵapanga iwowo ngati akapolo awo.

2. Pamene Mulungu anamaliza kupereka chilango kwa mitundu khumi ya ku Isirayeli ija, kodi Mulungu anayipatsa chilango chotani mitundu yiŵiri ya ku Yuda ija?
-Mulungu anatumiza anthu a ku Babeloni kuti akayiyambe mitundu yiŵiri ya ku Yuda, ndikuŵapanga iwowo kukhala akapolo awo.

3. Kodi anthu a ku Babeloni anawuwononga bwanji mzinda wa Yelusalemu?
-Anayiwotcha ndi moto Nyumba ya Mulungu.
-Anayiwotcha Yelusalemu yonse.
-Anagwetsa linga lozungulira mzinda wa Yelusalemu.

4. Kodi anthu a ku Yuda anachita chiyani atabweleranso ku Yelusalemu?
-Anamanganso Nyumba ya Mulungu.
-Anawumanganso mzinda wa Yelusalemu.
-Anamanganso linga lozungulira mzinda wa Yelusalemu.

5. Anthu a ku Yuda amene anabwelera ku Yelusalemu amkatchedwa ndi dzina latsopano.
-Dzina latsopano la anthu a ku Yuda linali Ayuda.

6. Kodi Mulungu anatumiza anthu a mitundu yiti iŵiri, kudzaŵayambanso Ayuda?
-Agiliki ndi Aloma.

7. Kodi Aloma ankapembedza chiyani?
-Aloma ankazipembedza zosema zambiri.

-Aloma ankayipembedza mfumu yawo, kayisala.

8. Kodi Alembi anali ndani?
-Alembi anali atsogoleri a Chiyuda amene amkalemba mawu a Mulungu.

9. Kodi Afarisi anali ndani?
-Afarisi anali atsogoleri a Chiyuda amene ankaphunzitsa mawu a Mulungu.

10. Kodi Asaduki anali ndani?
-Asaduki anali atsogoleri a Chiyuda amene anali olemera kwambiri ndipo ankayang'anira Nyumba ya Mulungu.

11. Kodi Masunagogi anali chiyani?
-Nyumba zimene Ayuda ankakomaniranamo ndi kumaŵerenga ndi kukambirana zolembedwa za Mose.

12. Kodi pa nthaŵi imeneyo, panali Ayuda amene ankakhulupilira mwa Mulungu?
-Inde, pang'ono.

-Mulungu anatumiza aneneri ambiri kudzalankhula kwa iwo.

-M'modzi mwa aneneri omaliza amene Mulunghu anaŵatumiza kudzalankhula kwa iwo anali Malaki.

-Malaki anaŵawuza Ayuda kuti Mulungu sanaŵayiwale iwo, ndipo adzatumiza Mpulumutsi.

-Malaki atamwalira, Mulungu sanalankhulenso kwa Ayuda kwa zaka 400.

-Chifukwa chakuti Ayuda ambiri sankakhulupilira mwa Mulungu, ochepa okha ndi amene ankayembekezera kuti



iye mwana wamamuna.

-Chomchonso zinali zosatheka kwa Mariya, namwali, kukhala ndi mwana, komanso Mulungu anamupatsa iye mwana wamamuna.

-Mulungu amatha kuchita china chilichonse.

-Palibe zisatheka ndi Mulungu.

-Kodi kenako Mariya anayankha chiyani?

Tiyeni tiŵerenge Luka 1:38

38-Ndipo Mariya anati, “Tawonani, ine ndi watchito wa Ambuye, zichitike kwa ine malingana ndi mawo Awo.” Kenako mngeloyo anachoka.

-Chifukwa chakuti Mariya anamukhulupilira Mulungu, Mulungu anamusankha iye kuti akhale mayi ake a Yesu, Mpulumutsi amene ankabwera.

-Kodi Yesu anakakhala Mpulumutsi wa mu lonjezo lja?
-Inde.

-Yesu anakakhala Mpulumutsi amene Mulungu analonjeza pachiyambi kwa Adamu ndi Hava m'munda mwa Edeni.

-Yesu anakhala Mpulumutsi amene Mulungu analonjeza kwa Abulahamu, Isaki, Yakobo ndi anthu onse.

-Kodi mngeloyo anayankha kuti chiyani?

-Mngeloyo anayankha kuti Mulungu Mzimu Woyera adzapanga zodabwitsa ndipo Mariya adzakhala ndi pathupi.

-Mwana wamamuna wa Mariya adzabadwa palibe mbewu ya munthu wa mamuna ndi mkazi.

-Kodi chifukwa chiyani mwana wamamuna wa Mariya anakabadwa palibe mbewu ya mamuna ndi mkazi?
-Chifukwa chakuti Iye akufunika kuti abadwe alibe tchimo la Adamu ndi Hava.
-Chifukwa chakuti Iye akufunika kuti abadwe ali olungamika ndiponso opanda tchimo.
-Chifukwa chakuti Mulungu Mwana adzabadwa ngati munthu koma opanda tchimo lina lililonse, Iye sadzakhala ndi mbewu ya bambo ndi mayi.

-Mwana wamamuna wa Mariya adzakhala mbewu ya Mulungu yokha.

-Kodi china ndi chiyani chimene analankhula mngelo, za mwana wamamuna wa Mariya, Mpulumutsi amene anakabwerayo?

Tiyeni tiŵerenge Luka 1:36-37

36-[Mngelo anati] "Ndiponso tawona m'bale wako, Elizabeti, ali ndi pathupi pa mwana wamamuna ku ukalamba wache; ndipo uno ndi mwezi wa chisano ndi umodzi, iye ankatchedwa kuti ndi osabereka.
37-Pakuti palibe chosatheka ndi Mulungu."

-Apa pali zimene analankhula mngelo:
-Ngati m'mene zinalili zosatheka kwa Elizabeti, okalamba kwambiri, mkazi osabereka, koma Mulungu anamupatsa



Mulungu adzatumiza mpulumutsi.

-Aŵiri mwa Ayuda amene ankayembekezera kuti Mulungu adzatumiza Mpulumutsi anali Zakariya ndi mkazi wache, Elizabeti.

-Zakariya anali wamsembe, chomcho iye pamodzi ndi mkazi wache ankamukhulupilira Mulungu.

-Koma Zakariya ndi mkazi wacheyo anali ndi vuto.

Tiyeni tiŵerenge Luka 1:7

7-Koma [ Zakariya ndi Elizabeti] analibe mwana, pakuti Elizabeti anali osabereka, ndiponso aŵiriwo anali okalamba.

-Kodi vuto la Zakariya ndi Elizabeti linali lotani?
-Analibe ana.

-Kodi chifukwa chiyani analibe ana?
-Chifukwa chakuti Elizabeti anali osabereka.
-Chifukwa chakuti Zakariya pamodzi ndi Elizabeti anali okalamba kwambiri.
-Chifukwa chakuti Zakariya wamsembe, ntchito yache inali yotumikira Mnyumba ya Mulungu ku Yelusalemu.

Tiyeni tiŵerenge Luka 1:8-9

8-Pamene Zakariya ankagwira ntchito ngati wamsembe pa maso pa Mulungu, ndiponso nthaŵi imeneyi inali yogwira ntchito anthu a gulu lawo.
9-Ngati khalidwe la anthu amsembe, mawula anamugwera Zakariya oloŵa Mkachisi wa Mulungu kukafukiza msembe zonunkhura.

-Pa tsiku limene Zakariya analoŵa Mnyumba ya Mulungu, mchipinda chopatulika, kukafukiza msembe zonunkhira kwa Mulungu, chinachake chinamuchitikira iye.

-Kodi chinamuchitikira ndi chiyani Zakariya pamene anali Mnyumba ya Mulungu ija?

Tiyeni tiŵerenge Luka 1:11-14

11-Ndipo mngelo wa Mulungu anamuwonekera iye, anayima kumanja kwa guwa lofukizira msembe zonunkhira.
12-Zotsatira zache iye anadabwa kwambiri atamuwona mngeloyo, ndipo anagwidwa ndi mantha.
13-Koma mngeloyo anati, “Usawope Zakariya, pakuti pemphero lako lamveka, mwakuti mkazi wako, Elizabeti adzakuberekera mwana wamamuna, ndipo udzamutcha dzina lakuti Yohane.
14-Udzakhala osangalala, ndiponso anthu ambiri adzasangalala chifukwa cha kubadwa kwache.”

-Mngelo wa Mulungu anamuwonekera Zakariya.

-Kodi mngeloyo anamuwuza chiyani Zakariya?
-Mngeloyo anamuwuza Zakariya kuti Mulungu ankafuna kumupatsa iye mwana wamamuna, ndipo dzina lake lidzakhala Yohane.

-Kodi kenako mngeloyo analankhula chiyani za mwana wamamuna amene Mulungu ankafuna kumupereka kwa Zakariya uja?

Tiyeni tiŵerenge Luka 1:15-17

15-[Mngelo anatinso] “Pakuti adzakhala wamkulu pa maso pa Ambuye, sadzamwa vinyo kapena zoledzeretsa.



-Mngelo analankhula kuti mwana wa Mariya , Mpulumutsi amene ankabwerayo, adzakhala chidzukulu cha mfumu Davide.

-Kodi chifukwa chiyani Mpulumutsi anabadwa mwa zidzukulu za Davide?
-Chifukwa chakuti Mulungu anapereka lonjezo kwa mfumu Davide kuti Mpulumutsi adzakhala m’modzi mwa zidzukulu zache.
-Chifukwa chakuti Mpulumutsi amene ankabwerayo adzakhala chidzukulu cha mfumu Davide, Mulungu adzamusankha Iye kukhala Mfumu ya ku Isirayeli ndipo adzakhala mfumu mpaka kalekale.

-Kodi kenako Maliya anamufunsa chiyani mngeloyo?

Tiyeni tiŵerenge Luka 1:34

34-Mariya anamufunsa mngeloyo kuti, “Kodi zimenezi zidzatheka bwanji, pakuti ine sindikumudziŵa mamuna?”

-Kodi funso la Mariya linali lotani?
-Mariya anafunsa za m’mene angathele kukhala ndi mwana chifukwa chakuti iye anali namwali.

-Kodi mngeloyo anayankha kuti chiyani?

Tiyeni tiŵerenge Luka 1:35

35-Mngeloyo anayankha kuti, “Mzimu Woyera udzatsikira pa iwe, ndipo mphamvu ya wa Wakumwamba idzabwera pa iwe; chomcho mwana amene adzabadweyo adzatchedwa kuti Woyera , Mwana wa Mulungu.”

-Mngelo uja analankhula kuti mwana wamamuna wa Mari-
ya, adzatchedwa kuti Mwana wa Wakumwamba.
-Kodi mngeloyo ankamasulira chiyani pamene ankanena kuti mwana wamamuna wa Mariya adzatchedwa kuti Mwana wa Wakumwamba?
-Mwana wamamuna wa Mariya adzakhala Mwana wa Mulungu.

-Kodi zidzatheka bwanji kuti mwana wamamuna wa Mariya kuti adzakhale Mwana wa Mulungu?
-Kodi Mulungu anabereka mwana?
-Iyayi.

-Kodi mukukumbukira kuti Mulungu alipo m'modzi, koma mwa m'modziyo alipo atatu?

-Mulungu ndi Mulungu Atate, Mulungu Mpulumutsi ndi Mulungu Mzimu Oyera.

-Mulungu Atate ndi Mulungu Mzimu Oyera ankamutumiza Mulungu Mpulumutsi pa dziko la pansi ngati Mwana wa Mulungu komanso mwana wa munthu.

-Mwana wamamuna wa Mariya adzakhala Mulungu komanso munthu.

-Kodi china ndi chiyani chimene analankhula mngelo, za mwana wamamuna wa Mariya, Mpulumutsi amene anakabwerayo?

Tiyeni tiŵerenge Luka 1:32b-33

32b-Ambuye Mulungu adzamuloŵetsa Iye pa mpan-
do wa ufumu wa atate ache, Davide.
33-ndipo adzaŵalamulira anthu a nyumba ya Yoko-
bo mpaka kalekale."



Ndiponso adzadzadzidwa ndi Mzimu Woyera, kuyambira akadzangobadwa.
16-Adzayitembenuza mitima ya a Isirayeli ambiri
kuti abwerere kwa Mulungu wawo.
17-Ndipo iye ndi amene adzayende patsogoro pa
Ambuye, mu mzimu ndi mphamvu za Mneneri Eliya, kwayanjanitsa makolo ndi ana awo, adzatembenuza mitima ya anthu osamva kuti akhale ndi mzeru za anthu olungamika, ndiponso kwapangitsa anthu kukonzeka za Ambuye.

-Mngeloyo analankhula kuti mwana wamamuna wa Zakariya, Yohane, adzaŵapangitsa anthu kukhala okonzeka pomudikilira Mpulumutsi amene ankabwerayo.

-Kodi mngeloyo anamutcha kuti ndani Mpulumutsi amene ankabwerayo?
-Ambuye.

-Kodi Ambuye ndi ndani?
-Ambuye ndi Mulungu.

-Mngeloyo analankhula kuti Mpulumutso amene ankabwerayo adzakhala Ambuye, Mulungu mwini.

-Zimenezi zitatha, Elizabeti, mkazi wache wa Zakariya anakhala ndi pathupi.

Tiyeni tiŵerenge Luka 1:24-25

24-Pambuyo pache mkazi wache anakhala ndi
pathupi, ndipo anazibisa kuti anthu asamuwone kwa miye-
zi isano akumati,
25-"Ambuye andithandiza ine kukhala ngati m'mene
ndikuwonekeramu, m'masiku ano andichitira chisoni pon-
dichotsera kusabereka kumene kumkandichititsa manyazi

pakati pa anthu.”

-Kenako Mulungu anatumiza mngelo kwa namwali otchedwa Maliya.

Tiyeni tiŵerenge Luka 1:26-31

26-Patapita miyezi yokwana isano ndi umodzi, chitengereni pathupi Elizabeti, Mulungu anamutuma mngelo Gabuliyeli kuti apite ku mzinda wotchedwa Nazaleti ku Galileya,

27-kwa namwali amene anali asanawonaneko ndi mamuna aliyense, amene anali pa chitomelo ndi mamuna wina wache, dzina lache Yosefe, wa mtundu wa Davide, namwaliyo, dzina lache linali Mariya.

28-Mngelo anafika kwa iye ndipo anati, “Mtendere ukhale ndi iwe, wokondedwa ndi Mulungu, Ambuye ali ndi iwe!”

29-Koma namwaliyo, anavutika mu mtima kwambiri chifukwa cha zimene mngeloyo analankhula, ndipo ankazifunsa yekha mu mtima, kumasulira kwa mawu a mngeloyo.

30-Mngeloyo anatinso kwa iye, “Usawope Mariya, pakuti chikondi cha Mulungu chakuwonekera iwe.

31-Ndiponso tawona, iwe udzakhala ndi pathupi ndipo udzabereka mwana wamamuna, ndipo udzamutcha dzina lache Yesu.”

-Kodi mngelo anamuwuza chiyani Maliya?
-Mngelo anamuwuza Maliya kuti Mulungu anamusankha iye kuti akhale mayi wa Mpulumutso amene ankabwerayo.

-Kodi Mulungu anayiŵala lonjezo lache lotumiza Mpulumutsi?
-Iyayi, Mulungu sanaliyiŵale lonjezo lache.



-Kodi chifukwa chiyani Mulungu analikumbukira lonjezo lache lotumiza Mpulumutsi?
-Chifukwa chakuti Mulungu amaŵakonda anthu onse.
-Chifukwa chakuti Mulungu ankafuna kuŵapulumutsa anthu onse ku mphamvu ya tchimo, imfa ndi Satana.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamusankha Mariya?
-Kodi ndimayesa kuti Mariya anali mwana wa Adamu ndi Hava?
-Inde.

-Kodi ndimayesa kuti Mariya anabadwira mu tchimo ngati anthu ena onse?
-Inde.

-Kodi nanga chifukwa chiyani Mulungu anamusankha Mariya?
-Chifukwa chakuti Mariya anamukhulupilira Mulungu.
-Chifukwa chakuti Mariya ankamuyembekezera Mulungu kuti atumize Mpulumutsi.

-Kodi dzina la mwana wa Mariya lidzakhala ndani?
-Yesu.

-Kodi dzina lakuti “Yesu” likumasulira chiyani?
-Dzina lakuti “…Yesu” likumasulira kuti “Mpulumutsi”.

-Kodi china ndi chiyani chimene analankhula mngelo, za mwana wamamuna wa Mariya, Mpulumutsi amene ankabwerayo?

Tiyeni tiŵerenge Luka 1:32a

32a-[Mngelo anati] “Iye adzakhala wamkulu, ndipo adzatchedwa kuti Mwana wa Mulungu Wakumwamba.”